



Kuphunzira Kudzera mu Masewera mu Maphunziro a Ana a Chichepere

NYANJA/CHEWA

Kodi kusewera ndi chiyani?

Maphunziro pa dziko lonse lapansi aonetsa kuti ana amaphunzira ndi kukula pamene akuchitanso masewera owathandiza pa moyo wawo.

“Kusewera ndikofunika poti kumathandizira kuti mwanayo akule bwino mu nzeru, mwa thupi, mkuyanjana ndi ena komanso mukukhala ndi zochitachita. Njira zabwino za kuphunzitsira ana a chichepere zimagwiritsa ntchito njira za kusakaniza kuphunzitsa ndi kuphunzira komwe kumathandiza kugawana zochitika pakati pa ophunzitsa ndi ana. Kudzera mwa kusewera ndi danga, ana amaphunzira kuganizira kupanga ziganizo zomveka za kucheza komanso za dziko, anthu, malo, zinthu, ndi zimene amakumana nazo pa moyo wa tsiku ndi tsiku.”

- VEYLDF, 2016, tsamba 14

Kusewera mwa mwana wanu kumangobwera mwachilengedwe ndipo ndi gawo lofunikira pa kuphunzira ndi kukula kwawo. Kusewera kumathandiza mwana wanu kudziwa ndi kuzindikira bwino dziko limene ali ndikupitiriza kukulitsa kudziwa. Kudzera m’kusewera, mwana wanu akhoza kuyerekeza, kuyesa, kupanga, kufuna kupeza, kufufuza, kulumikizana ndi ena, kufunsa, kulankhula, kumvetsera, kuganiza, kumva, kugwira ndi kununkhiza. Pakusewera pali kukambirana ndi kugwirizana, kuthetsa vuto, kutenga chiopsezo, kuyesa zinthu zatsopano, ndi kuona m’mene zinthu zigwirira ntchito. Mwana wanu adzaphunzira za iye yekha ndi anzake, kuphunzira malamulo a kusewera, kupanga ubwenzi, kupanga ubale ndi kudalira pa ena omuzungulira kuphatikizapo omuphunzitsa ndi anzake.

Ana nthawi zina amasewera wokha, kapena ndi wina kapena ena awiri ndiponso kusewera mumagulu ang’ono kapena akulu a ana. Kusewera kukhoza kukhala kwa phokoso kapena kwa chete, kopanda machitachita kapena kojijirika.

“Nthawi imene ana amakhala akusewera kopanda kuwasokoneza, kumawapatsa nthawi ya kupanga zatsopano, kufufuza ndi kupeza, pogwiritsa ntchito zinthu zambiri zosiyanasiyana, poganizira za zinthu zosiyanasiyana ndi kuzigwiritsa ntchito.”

- VEYLDF, 2016, tsamba 21

Kuphunzira Kudzera mu Masewera

Aphunzitsi ndi ena ophunzitsa akhoza kupanga pulogalamu yokhudzana ndi zofuna za mwana wina aliyense amene akufuna thandizolo. Amachita ichi mwakulola njira zambiri za kusewera ndi kuphunzira pa malo amenewo pomwe ana akhoza kuyenda momasuka m’kati mwa chipinda kapena kunja.

Kudzakhala zochitika zoikika monga, kuyimba nyimbo, nthano ndi kukambirana. Kwa nthawi yaikulu ya tsiku, ana adzakhala akupanga maganizo awo a komwe adzafuna kukasewera, amene adzasewera nawo, komanso kusewera mwa nthawi yotalika motani pa masewera amenewo osankhidwa. Ophunzitsa adzapereka thandizo ndi chiunikiro pomwe ana akufuna thandizo.

Ophunzitsa adzagwiritsa ntchito njira zosiyanasiyana zophunzitsira pofuna kuthandiza ana kuti akhale akukonda kuphunzira, kufunsa, kufuna kudziwa ndi kukhala ndi chidwi pakati pawo ndi pakati pa anthu okumana nawo. Mwina akhoza kupereka chiunikiro pa masewera, kutsogolera kusewera, kapena kuonerera ana akuchita masewera awo otsogoleredwa.

Kodi ana amaphunzira chiyani akamasewera?

Kusewera kumapereka danga kwa ana la kulankhulana ndi kufunsa mafunso, kutukula ndi kunena mawu mobwerezabwereza a chilankhulo, kuwerenga, manambala, ndi kukhala ndi luso lakuchita zinthu mogwirizana. Kudzera mu kusewera, ana akuphunzira mmene angalumikizirane ndi kugwirizirana bwino ndi anthu ena.

Ana nawonso amagwiritsa ntchito maganizo ongyerekeza kuchita zomwe aona, mwachitsanzo;

- Kuyeserera kukonza zakudya
- Kusamalira mwana
- Kukhala wozimitsa moto, dokotala kapena wogulitsa musitolo.

Ichi chimathandiza ana kumvetsa ndi kuzindikira zinthu zowazungulira m'malo amene akukhala.

“Masewera a zitsuzo ndiwofunikira koposa pakufufuza zinthu zosiyanasiyana ndi ziganizo zosiyana, kudzanso maganizo a kukhala m'magulu a padziko lonse lapansi. Ana ayenera kuthandizidwa kuyamikira kufanana ndi kusiyana komwe kulipo pakati pa anthu ndi magulu a anthu, ndi kulemekeza maganizo osiyanasiyana.”

- VEYLDF, 2016, tsamba 18

Pomwe mwana wanu akusewera, adzakambirana za malamulo kuwathandiza kuphunzira za makhalidwe amene ali ovomerezeka kwa ena. Mwachitsanzo, ana akhoza kupanga malamulo a kuyembekezera kuti nthawi yawo ifike yakusonjola. Kulola ana kutenga mbali pa kupanga malamulo othandiza aliyense kukhala wotetezeka, kusamalira zida, komanso kuthandiza kuti pakhale ubwino ndi kusakondera, kudzathandiza kuganiza kwao komanso mmene angathetsere vuto, ndipo izizi zidzathandizanso pakulimbikitsa luso la kukambirana kwao, luso la mgwirizano, ndi luso la kuwerengera manambala ndi mawu.

Pa masewera awo, ana akhoza kugwiritsa ntchito ndi kupyozapo pa nzeru zomwe ali nazo kale ndi kuchita zatsopano mwa njira yochititsa chidwi.

Ana akhoza kuchita zinthu zina mobwerezabwereza, mosasamalira za chiopsezo chilipo ndi kuphunzira ndi kuchita zinthu zimenezo, monga;

- wokha kukwera pa malo a pamwamba kwambiri
- kudziwa kulumikiza zidutsa za chinthu china chake kuti chikhale cha thunthu bwino
- kuvala wokha zobvala zawo kapena kuvala zina pamwamba
- kuyenda pamalo povuta koma osagwa
- kugwiritsa ntchito sizala
- kulumphalumphu
- kudzikankha okha polendewera.

Zochita zonsezi, zazikulu ndi zazing'ono, ndi mphoto kwa ana, mabanja awo komanso kwa ophunzitsa womwe akuwathandiza kuphunzira.

Kusewera kumapatsa ana danga la, kusangalala, kukwaniritsa, kupambana, kuphonya, kuchita mobwereza, kuyesa mfundo zatsopano kapena maluso, kupanga ziganizo ndi kuchita maluso atsopano komanso kupeza nzeru.

Kusewera ndimo m'mene mwana aphunzirira.

Maumboni

Department of Education and Training, 2016. *Victorian Early Years Learning and Development Framework*.